

# العلوم الإسلامية

لغير الناطقين بالعربية

المستوى الأول

الحديث الشريف

باللغة التليثيوية



تأليف

وحياتين عبد السلام باالي




# MAPHUNZIRO A CHISILAMU

K wa Olankhulo Zina  
Posakhala Chi Arab

Kalasi 1

Hadith

Mchiyankhulo cha Chichewa



Olemba:

Waheed Abdul Salam Baali



# MAPHUNZIRO A CHISILAMU

K wa Olankhula Zilankhulo  
Zina Posakhala Chi Arab

**Kalasi 1**

**[ Hadith ]**

Mchiyankhulo cha Chichewa

Olemba:

Waheed Abdul Salam Baali

العلوم الإسلامية

لغير الناطقين بالعربية

المستوى الأول

الحديث الشريف

باللغة الشيشيوية

تأليف

وحيد بن عبد السلام بن باني

# HADITH

(Zoyankhula za  
Mtumiki<sup>(s.a.w)</sup>)

K wa Olankhula Zilankhulo  
Zina Posakhala Chi Arab

## Kalasi 1

Mchiyankhulo cha Chichewa

Olemba:

Waheed Abdul Salam Baali

# فَتْحُ الْحَدِيثِ

لِغَيْرِ النَّاطِقِينَ بِالْعَرَبِيَّةِ

الْمُسْتَوَى الْأَوَّلُ

بِاللُّغَةِ الشَّيْشِيَوِيَّةِ

تَأليف

وحيد بن عبد السلام بن بآلي

## Mau Oyamba

Kuyamikidwa konse ndi kwa Mulungu, Mtendere ndi Madalitso zikhale pa Mtumiki Muhammad, akubanja lake ndi ma Sahabah ake onse.

Kuphunzita malamulo a Chisilamu ndi ntchito yabwino kwambiri pa maso pa Mulungu ndipo ngati ophunzira agwiritse ntchito zomwe aphunzirazo, mphunzitsi amalipidwa mofanana ndi ophunzirayo.

**Mu Hadith yomwe anailandira Muslim, Mulungu asangalale naye, anamva kuchokera kwa Abu Hurairah yemwe anati, Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati: "yemwe waitanira ku chiwongoko, amalandira malipiro ofanana ndi yemwe watsatirayo ndipo sikapunguka kena kalikonse mmalipirowo" Sahih Al Bukhari 4/2060.**

Choncho munthu ophunzitsa akuyenera kutsimikiza kugwira ntchitoyi ndi cholinga choziyandikitsa kwa Mulungu kuti apeze chisangalalo chake komanso akaikidwe ku Mtendere.

Tikufunira Mtendere ndi Madalitso zochokera kwa Mulungu, zipite kwa Mtumiki Muhammad, akubanja lake ndi ma Sahabah ake onse.

Olemba:

Waheed Abdul Salam Baali

Dedza-Malawi

Loweruka, pa 29 Dhul Qa'dah 1434

## مُقَدِّمَةٌ

الْحَمْدُ لِلَّهِ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى رَسُولِ اللَّهِ وَعَلَى آلِهِ وَأَصْحَابِهِ أَجْمَعِينَ وَبَعْدُ،

فَإِنَّ تَعْلِيمَ أَحْكَامِ الْإِسْلَامِ مِنْ أَفْضَلِ الْأَعْمَالِ عِنْدَ اللَّهِ، وَكُلَّمَا عَمِلَ الْمُتَعَلِّمُ بِهَا عِلْمَهُ كُتِبَ لَكَ مِثْلُ أَجْرِهِ.

فَقِي صَحِيحِ مُسْلِمٍ عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ، أَنَّ رَسُولَ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ، قَالَ: «مَنْ دَعَا إِلَى هُدًى، كَانَ لَهُ مِنَ الْأَجْرِ مِثْلُ أُجُورِ مَنْ تَبِعَهُ، لَا يَنْقُصُ ذَلِكَ مِنْ أُجُورِهِمْ شَيْئًا (١)»

فَيَتَّبِعِي لِلْمُدَرِّسِ أَنْ يَنْوِيَ التَّقَرُّبَ إِلَى اللَّهِ بِهَذَا الْعَمَلِ لِيَتَّالِ رِضَا اللَّهِ وَجَنَّتْهُ

وَصَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ وَعَلَى آلِهِ وَأَصْحَابِهِ أَجْمَعِينَ

كُتِبَ / وحيد بن عبد السلام بن بالي

دَوْلَةُ مَالَاوِي - دِيدَزَا

يوم السبت ٢٩ من ذي القعدة سنة ١٤٣٤ هـ

(١) صحيح: رواه مسلم (٤/ ٢٠٦٠)

## Njira Yophunzitsira

1. Mphunzitsi wa Chiluya awerenge pang'onopang'ono komanso momveka bwino, ndipo ophunzira amutsatire.
2. Mphunzitsi wa Chiluya awerenge gawo lirilonse katatu-katatu ndipo ophunzirawo adzimutsatira kuwerenga kulikonse.
3. Mphunzitsi wa Chiluya alongosole phunziro ndipo mmodzi wa omasulira amasulire kwa ophunzira omwe sakumva chi Arab.
4. Mphunzitsi wa Chiluya awerenge kachiwiri gawo lirilonse katatu-katatu, ndipo ophunzirawo adzimutsatira kuwerenga kulikonse.
5. Ophunzira aliyense aimilire ndikuwerenga ndipo mphunzitsi adzimukhonza zolakwika zake mpaka akwanitse.
6. Pa maphunziro a Wudhu, Adhan ndi Swalat, mphunzitsi wa Chiluya apange zonsezo pa maso pa ophunzira, ndipo ophunzirawo apange mmodzimodzi.
7. Kenako mphunzitsi wa chi Malawi aphunzitse ophunzira ake monga mmene waphunzilira.

\*\*\*

## طَرِيقَةُ التَّدْرِيسِ

- ۱- يَقُومُ الْمُدَرِّسُ الْعَرَبِيُّ بِقِرَاءَةِ الدَّرْسِ أَمَامَ الْمُدَرِّسِينَ الْمَحَلِّينَ ثَلَاثَ مَرَّاتٍ بِصَوْتٍ وَاضِحٍ وَبِبَطْءٍ .
- ۲- يَقْرَأُ الْمُدَرِّسُ الْعَرَبِيُّ كُلَّ فُقْرَةٍ ثَلَاثَ مَرَّاتٍ وَهُمْ يُرَدِّدُونَ خَلْفَهُ كُلَّ مَرَّةٍ .
- ۳- يَقُومُ الْمُدَرِّسُ الْعَرَبِيُّ بِشَرْحِ الدَّرْسِ وَيَقُومُ أَحَدُ الْمُتَرْجِمِينَ بِتَرْجُمَتِهِ لِمَنْ لَا يُجِيدُ الْعَرَبِيَّةَ مِنَ الْمُدَرِّسِينَ .
- ۴- يَقْرَأُ الْمُدَرِّسُ الْعَرَبِيُّ كُلَّ فُقْرَةٍ ثَلَاثَ مَرَّاتٍ وَهُمْ يُرَدِّدُونَ خَلْفَهُ مَرَّةً أُخْرَى .
- ۵- يَقُومُ كُلُّ وَاحِدٍ يَقْرَأُ الدَّرْسَ وَالْمُدَرِّسُ يُصَحِّحُ لَهُ حَتَّى يُتَقِنَ قِرَاءَتَهُ .
- ۶- فِي دُرُوسِ الْوُضُوءِ وَالصَّلَاةِ وَالْأَذَانِ يَقُومُ الْمُدَرِّسُ الْعَرَبِيُّ بِذَلِكَ عَمَلِيًّا أَمَامَهُمْ ثُمَّ يَفْعَلُونَهُ وَاحِدًا وَاحِدًا .
- ۷- يَقُومُ الْمُدَرِّسُ الْمَحَلِّيُّ بِإِعْطَاءِ الدَّرْسِ لِطُلَابِهِ بِنَفْسِ الطَّرِيقَةِ الَّتِي تَلَقَّاهُ بِهَا .

\*\*\*

**1. Pemphero Lonena Polowa mu Chimbudzi**  
Mu Hadith yomwe anailandira Al Bukhari ndi Muslim, Anasi (Mulungu asangalale naye) anati: Mtumiki wa Mulungu Mtendere ndi Madalitso zikhale pa iye amati akamalowa mu chimbudzi, amanena mau awa: "Allahumma Inni A'udhu bika minal khubthi wal khabaith" Al Bukhari 142 – Muslim375

**2. Pemphero Lonena Potuluka mu Chimbudzi**  
At Tirmidh ananena mu Hadith yomwe inachokera kwa Aisha Mulungu asangalale naye, anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye amati akamatuluka mu chimbudzi, ankanena mau awa: "Ghufraanaka" At Tirmidhi 7, Abu Daud anati ndi yabwino koma yachilendo: 30

**3. Pemphero Lonena pa Nthawi ya Mavuto**  
Mu Hadith yomwe anailandira Al Bukhari ndi Muslim, Ibn Abbas Mulungu asangalale naye anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anali kunena mau awa nthawi ya mavuto: "Laa ilaaha illa

Allah al-Adheem al-Haleem, laa ilaaha illa Allah Rabbul Arsh al-Adheem, laa ilaaha illa Allah Rabbu ssamawaat wa Rabbul Ardhi wa Rabbul Arshil-Kareem" Al Bukhari 5996 - Muslim 5016

#### ١ - دُعَاءُ دُخُولِ الْخَلَاءِ

فِي الصَّحِيحَيْنِ عَنْ أَنَسٍ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ قَالَ كَانَ النَّبِيُّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ إِذَا أَرَادَ أَنْ يَدْخُلَ الْخَلَاءَ قَالَ اللَّهُمَّ إِنِّي أَعُوذُ بِكَ مِنَ الْخُبْثِ وَالْخَبَائِثِ<sup>(١)</sup>

#### ٢ - دُعَاءُ الْخُرُوجِ مِنَ الْخَلَاءِ

رَوَى التِّرْمِذِيُّ وَحَسَنَهُ عَنْ عَائِشَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهَا قَالَتْ كَانَ النَّبِيُّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ إِذَا خَرَجَ مِنَ الْخَلَاءِ قَالَ غُفْرَانُكَ<sup>(٢)</sup>

#### ٣ - دُعَاءُ الْكَرْبِ

فِي الصَّحِيحَيْنِ عَنْ ابْنِ عَبَّاسٍ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا أَنَّ رَسُولَ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ كَانَ يَقُولُ عِنْدَ الْكَرْبِ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ الْعَظِيمُ الْحَلِيمُ لَا إِلَهَ إِلَّا رَبُّ السَّمَوَاتِ وَرَبُّ الْأَرْضِ وَرَبُّ الْعَرْشِ الْكَرِيمِ<sup>(٣)</sup>

(١) صحيح: رواه البخاري (١٤٢) ومسلم (٣٧٥)  
(٢) حسن: رواه الترمذي (٧) وقال حسن غريب وأبو داود (٣٠)

(٣) صحيح: رواه البخاري (٥٩٩٦) ومسلم (٥٠١٦)

#### ٤ - الدُّعَاءُ قَبْلَ إِيْتَانِ الزَّوْجَةِ

فِي الصَّحِيحَيْنِ عَنِ ابْنِ عَبَّاسٍ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا أَنَّ النَّبِيَّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ قَالَ: "لَوْ أَنَّ أَحَدَكُمْ إِذَا أَتَى أَهْلَهُ، قَالَ: بِاسْمِ اللَّهِ، اللَّهُمَّ جَنِّبْنَا الشَّيْطَانَ وَجَنِّبِ الشَّيْطَانَ مَا رَزَقْتَنَا، فَقَضَى بَيْنَهُمَا وَلَدٌ لَمْ يَضُرَّهُ". (١)

#### ٥ - كَيْفَ يُرَدُّ السَّلَامُ عَلَى الْكَافِرِ إِذَا سَلَّمَ

فِي الصَّحِيحَيْنِ عَنْ أَنَسِ بْنِ مَالِكٍ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ، قَالَ: قَالَ النَّبِيُّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ: "إِذَا سَلَّمَ عَلَيْكُمْ أَهْلُ الْكِتَابِ، فَقُولُوا: وَعَلَيْكُمْ". (٢)

#### ٦ - الدُّعَاءُ عِنْدَ سَمَاعِ صِيَاحِ الدِّيَكَةِ وَنَهْيِ الْحِمَارِ

فِي الصَّحِيحَيْنِ عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ، أَنَّ النَّبِيَّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ قَالَ: "إِذَا سَمِعْتُمْ صِيَاحَ الدِّيَكَةِ فَاسْأَلُوا اللَّهَ مِنْ فَضْلِهِ فَإِنَّهَا رَأَتْ

(١) صحيح: رواه البخاري (١٣٨)

(٢) صحيح: رواه البخاري (٦٢٥٨) ومسلم (٢١٦٣)

4. **Pemphero Lonena Tisanakhale Pamodzi ndi Mkazi**  
Mu Hadith yomwe anailandira Al Bukhari ndi Muslim, Ibn Abbas Mulungu asangalale naye anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati: "Mmodzi wa inu akanena mau awa pokumana ndi mkazi wake {Bismillah, Allahumman jannibna Asshaytaan, wa jannib Asshaytaan maa razaqtanaa, amapatsidwa mwana wotetezedwa ku shaytan}" Al Bukhari 138

5. **Munthu Osakhulupilira akapereka Salam Akuyenera Kuyankhidwa Bwanji?**

Mu Hadith yomwe anailandira Al Bukhari ndi Muslim, Anas bin Malik Mulungu asangalale naye anati, Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati: "Akakupatsani salam Mkhristu kapena Myuda, munene kuti: Wa'laikum" Al Bukhari 6258 – Muslim 2163

6. **Pemphero Lonena Tikamva Kulira kwa Tambala kapena Bulu**

Mu Hadith yomwe anailandira Al Bukhari ndi Muslim, Abu Hurairah Mulungu asangalale naye anati Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati: "Mukamva kulira kwa tambala, mupempheni Mulungu zabwino chifukwa

amakhala kuti waona Mngelo. Ndipo mukamva kulira kwa bulu, zitchinjirizeni kwa Mulungu kuchokera kwa Shaytan, chifukwa amakhala kuti waona shaytan" Al Bukhari 6558 – Muslim 2163

7. Ubwino wa Kupanga Tasbih (subhanallah), Tahmid (alhamdulillah) komanso Tahlil (laa ilaaha illa Allah)

Mu Hadith yomwe anailandira Al Bukhari ndi Muslim, Abu Hurairah Mulungu asangalale naye anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati: "Yemwe anganene 'Laa Ilaaha Illa Allah kokwana zana limodzi (100) tsiku lirilonse, Mulungu amuchotsera machimo ake onse, ngakhale kuchuluka kwake kutafanana ndi thovu la mu nyanja" Al Bukhari 3058 – Muslim 4908

8. At Tashahhud (Mau Omaliza pa Swalat)

Mu Hadith yomwe anailandira Al Bukhari ndi Muslim, Abdullah ibn Mas'ud Mulungu asangale naye anati: tinali tikumanena At Tahiyatu pa swalat kenako timadzuka nkumagwirana manja wina ndi mzake. Kenako Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anamva zimenezi ndipo anati: "Mudzinena kuti: 'Attahiyyaatu lillah, wasswalawaatu watwayyibaatu, assalam alaika ayyuha Nnabiyyu warahmatullah wabaraakatuh, assalam alaina wa 'ala ibaadillah sswaliheen. Ash'hadu anlaa ilaaha illa Allah, wa ash'hadu anna Muhammadan abduhu warasuluh.' Ndipo

مَلَكًا، وَإِذَا سَمِعْتُمْ نَهْيَ الْجَمَارِ فَتَعَوَّدُوا بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ، فَإِنَّهُ رَأَى شَيْطَانًا". (١)

٧- فَضْلُ التَّسْبِيحِ وَالتَّحْمِيدِ، وَالتَّهْلِيلِ

فِي الصَّحِيحَيْنِ عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ، أَنَّ رَسُولَ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ قَالَ: "مَنْ قَالَ: سُبْحَانَ اللَّهِ وَبِحَمْدِهِ فِي يَوْمٍ مِائَةَ مَرَّةٍ، حُطَّتْ خَطَايَاهُ، وَإِنْ كَانَتْ مِثْلَ زَبَدِ الْبَحْرِ". (٢)

٨- التَّشَهُُّدُ

فِي الصَّحِيحَيْنِ عَنْ عَبْدِ اللَّهِ بْنِ مَسْعُودٍ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ، قَالَ: "كُنَّا نَقُولُ التَّحِيَّةَ فِي الصَّلَاةِ وَنُسَمِّي وَنُسَلِّمُ بَعْضُنَا عَلَى بَعْضٍ، فَسَمِعَهُ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ فَقَالَ: قُولُوا: التَّحِيَّاتُ لِلَّهِ وَالصَّلَوَاتُ وَالطَّيِّبَاتُ السَّلَامُ عَلَيْكَ أَيُّهَا النَّبِيُّ وَرَحْمَةُ اللَّهِ وَبَرَكَاتُهُ السَّلَامُ عَلَيْنَا وَعَلَى عِبَادِ اللَّهِ الصَّالِحِينَ، أَشْهَدُ أَنْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ وَأَشْهَدُ أَنَّ مُحَمَّدًا عَبْدُهُ وَرَسُولُهُ، فَإِنَّكُمْ

(١) صحيح: رواه البخاري (٣٠٥٨) ومسلم (٤٩٠٨)

(٢) صحيح: رواه البخاري (٦٤٠٥) ومسلم (٢٦٩١)

mukapanga zimenezi, ndiye kuti mwafunira mtendere kapolo wina aliyense wochita zabwino kumwamba ngakhale panso" Al Bukhari 1127 – Muslim 609

#### 9. Mau Onena Podzuka ku Tulo

Hadith inachokera kwa Al Bukhari yemwe anamva kuchokera kwa Hudhaifah Mulungu asangalale naye, anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye amati akafuna kugona, amanena kuti: "Bismika Allahumma amutu wa ahya" ndipo akadzuka ku tulo amanena kuti; "Alhamdulillah iladhi ahyaana ba'da maa amaatanaa wa ilaih nnushur" Al Bukhari 6324

#### 10. Pemphero Lonena pa Sujuud

Nkhani inachokera kwa Al Bukhari, Aisha Mulungu asangalale naye anati: "Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anali kunena mau awa pa kuwerama ndi pa Sujud: "Subhanaka Allahumma Rabbanaa wabihamdika, Allahumma ighfir li" Al Bukhari 752

إِذَا فَعَلْتُمْ ذَلِكَ فَقَدْ سَلَّمْتُمْ عَلَى كُلِّ عَبْدٍ لِلَّهِ صَالِحٍ فِي السَّمَاءِ وَالْأَرْضِ  
(١)"

#### ٩ - أَذْكَارُ الْاِسْتِيقَاطِ مِنَ النَّوْمِ

رَوَى الْبُخَارِيُّ عَنْ حُذَيْفَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ قَالَ كَانَ النَّبِيُّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ إِذَا أَرَادَ أَنْ يَنَامَ قَالَ بِاسْمِكَ اللَّهُمَّ أَمُوتُ وَأَحْيَا وَإِذَا اسْتَيْقَظَ مِنْ مَنَامِهِ قَالَ الْحَمْدُ لِلَّهِ الَّذِي أَحْيَانَا بَعْدَ مَا أَمَاتَنَا وَإِلَيْهِ النُّشُورُ (٢)

#### ١٠ - دُعَاءُ السُّجُودِ

رَوَى الْبُخَارِيُّ عَنْ عَائِشَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهَا قَالَتْ كَانَ النَّبِيُّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ يَقُولُ فِي رُكُوعِهِ وَسُجُودِهِ سُبْحَانَكَ اللَّهُمَّ رَبَّنَا وَبِحَمْدِكَ اللَّهُمَّ اغْفِرْ لِي. (٣)

(١) صحيح: رواه البخاري (١١٢٧) ومسلم (٦٠٩)

(٢) صحيح: رواه البخاري (٦٣٢٤)

(٣) صحيح: رواه البخاري (٧٥٢)

# ١١ - الدُّعَاءُ إِذَا نَزَلَ الْمَطَرُ

رَوَى الْبُخَارِيُّ عَنْ عَائِشَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهَا، " أَنَّ رَسُولَ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ كَانَ إِذَا رَأَى الْمَطَرَ، قَالَ: اللَّهُمَّ صَيِّبًا نَافِعًا. (١)

## ١٢ - دُعَاءُ الْعُطَاسِ

رَوَى الْبُخَارِيُّ عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ، عَنِ النَّبِيِّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ قَالَ: " إِذَا عَطَسَ أَحَدُكُمْ فَلْيَقُلِ الْحَمْدُ لِلَّهِ، وَلْيَقُلْ لَهُ صَاحِبُهُ يَرْحَمُكَ اللَّهُ، فَإِذَا قَالَ لَهُ: يَرْحَمُكَ اللَّهُ، فَلْيَقُلْ يَهْدِيكُمْ اللَّهُ وَيُصْلِحْ بِالْكُفِّ (٢)."

## ١٣ - الدُّعَاءُ عِنْدَ الصُّعُودِ وَالْهَبُوطِ

رَوَى الْبُخَارِيُّ عَنْ جَابِرِ بْنِ عَبْدِ اللَّهِ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا، قَالَ: " كُنَّا إِذَا صَعِدْنَا كَبَّرْنَا، وَإِذَا نَزَلْنَا سَبَّحْنَا. (٣)

(١) صحيح: رواه البخاري (٩٧٤)

(٢) صحيح: رواه البخاري (٥٧٥٦)

(٣) صحيح: رواه البخاري (٢٧٧١)

# 11. Pemphero Lonena Mvula Ikagwa

Nkhani inachokera kwa Al Bukhari, Aisha Mulungu asangalale naye anati: "Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anali akunena mau awa akaona mvula: "Allahuma swayyiban naafi'an" Al Bukhari 974

## 12. Pemphero Lonena Poyetsemula

Nkhani inachokera kwa Al Bukhari, Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati: "Mmodzi wa inu akayetsemula, anene kuti 'Alhamdulillah' ndipo mzake anene

kuti 'yarhamka Allah', akamuyankha kuti yarhamka Allah, anene kuti 'yahdeekum Allah wayaslih baalakum'" Al Bukhari 5756

## 13. Pemphero Lonena Pokwera ndi Potsika

Nkhani inachokera kwa Al Bukhari, yemwe anamva kuchokera kwa Jabir Mulungu asangalale naye, akunena kuti: "Pamene tinali kukwera, tinkapanga takbir, ndipo potsika tinkapanga tasbih" Al Bukhari 2771

١٤ - تَلْقِينُ الْمُخْتَضِرِ

رَوَى مُسْلِمٌ عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ قَالَ : قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ لَقِّنُوا مَوْتَاكُمْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ (١)

١٥ - دُعَاءُ الرِّيحِ

رَوَى مُسْلِمٌ عَنْ عَائِشَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهَا زَوْجَ النَّبِيِّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ أَنَّهَا قَالَتْ : كَانَ النَّبِيُّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ إِذَا عَصَفَتِ الرِّيحُ، قَالَ : " اللَّهُمَّ إِنِّي أَسْأَلُكَ خَيْرَهَا وَخَيْرَ مَا فِيهَا وَخَيْرَ مَا أُرْسِلَتْ بِهِ، وَأَعُوذُ بِكَ مِنْ شَرِّهَا وَشَرِّ مَا فِيهَا وَشَرِّ مَا أُرْسِلَتْ بِهِ " (٢)

١٦ - الدُّعَاءُ إِذَا نَزَلَ مَنْزِلًا فِي سَفَرٍ أَوْ غَيْرِهِ

رَوَى مُسْلِمٌ عَنْ خَوْلَةَ بِنْتِ حَكِيمٍ السُّلَمِيَّةِ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهَا أَنَّهَا سَمِعَتْ رَسُولَ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ يَقُولُ : " إِذَا نَزَلَ أَحَدُكُمْ مَنْزِلًا، فَلْيَقُلْ

(١) صحيح : رواه مسلم (٩١٧)

(٢) صحيح : رواه مسلم (١٥٤٤)

14. Kuyankhulitsa Yemwe Imfa Yamudzera

Nkhani inachokera kwa Muslim, yemwe anamva kuchokera kwa Abu Hurairah akunena tumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati: "Yankhulitsani yemwe akufa mwa inu mau oti Laa ilaaha illa Allah" Muslim 917

15. Pemphero Lonena Nthawi ya Mphepo

Nkhani inachokera kwa Muslim, yemwe anamva kuchokera kwa Aisha Mulungu asangalale naye, akunena kuti: "Ikawomba mphepo, Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye amanena kuti: "Allahumma inni as'aluka khairaha, wa khaira maa fiha, wa khaira maa ursilat bihi. Wa audhu bika min sharriha, wa sharri maa fiha, wa sharri maa ursilat bih".

16. Pemphero Lonena Munthu akafika pa Nyumba Kuchokera ku Ulendo Wake kapena kulikonse.

Nkhani inachokera kwa Muslim yemwe anamva kuchokera kwa Khaula bint Hakim As Sulaimiyyah, Mulungu asangalale naye, iye anamva Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye akunena kuti

"Mmodzi mwa inu akafika pa nyumba yake, anene mau awa:

'Audhu bikalimaatillahi taammaat min sharri maa khalaqa' ndithu iyeyo sadzakhunziswa ndi choipa kufikira pamene watha ulendo wake" Muslim 4882

#### 17. Kufalitsa Mtendere (Salam)

Nkhani inachokera kwa Muslim yemwe anamumva Abu Hariarah, Mulungu asangalale naye, akunena kuti: Ananena Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye kuti: "Simudzalowa ku Mtendere mpaka mutakhulupilira, ndipo simungakhale okhulupilira pokhapokha mutayamba mwakondana. Ndikuuzani chinthu choti mukachita mukondana: Falitsani Mtendere (Salam) pakati panu" Muslim 81

#### 18. Pemphero Lonena Pomaliza Kudya

Nkhani inachokera kwa Abu Daud ndipo Al-Baani anaivomereza kuti ndiyoona, anamva kuchokera kwa Abu Ayyub Al Ansari, Mulungu asangalale naye, anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye amati akadya kapena kumwa, amanena kuti: "Alhamdulillah lladhi at'ama, wasaqaa, washawwaghahu, waja'la lahu makhrajan" Abu Daud 3/366 - Al Albani 3851

أَعُوذُ بِكَلِمَاتِ اللَّهِ التَّامَّاتِ مِنْ شَرِّ مَا خَلَقَ ، فَإِنَّهُ لَا يَضُرُّهُ شَيْءٌ حَتَّى يَرْجُلَ مِنْهُ " (١).

#### ١٧ - إِفْشَاءُ السَّلَامِ

رَوَى مُسْلِمٌ عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ ، قَالَ : قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ : " لَا تَدْخُلُونَ الْجَنَّةَ حَتَّى تُؤْمِنُوا ، وَلَا تُؤْمِنُوا حَتَّى تَحَابُّوا أَوَّلًا ، أَدْلَكُكُمْ عَلَى شَيْءٍ إِذَا فَعَلْتُمُوهُ تَحَابَبْتُمْ ، أَفْشُوا السَّلَامَ بَيْنَكُمْ " (٢).

#### ١٨ - الدُّعَاءُ عِنْدَ الْفَرَاغِ مِنَ الطَّعَامِ

رَوَى أَبُو دَاوُدَ وَصَحَّحَهُ الْأَلْبَانِيُّ عَنْ أَبِي أَيُّوبَ الْأَنْصَارِيِّ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ ، قَالَ : كَانَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ إِذَا أَكَلَ أَوْ شَرِبَ قَالَ : «الْحَمْدُ لِلَّهِ الَّذِي أَطْعَمَ ، وَسَقَى وَسَوَّغَهُ وَجَعَلَ لَهُ مَخْرَجًا» (٣).

(١) صحيح : رواه مسلم (٤٨٨٢)

(٢) صحيح : رواه مسلم (٨١)

(٣) صحيح : رواه أبو داود (٣/٣٦٦) وصححه الألباني (٣٨٥١)

١٩ - الدُّعَاءُ عِنْدَ إِدْخَالِ الْمَيِّتِ الْقَبْرِ

رَوَى أَبُو دَاوُدَ بِسَنَدٍ صَحِيحٍ عَنْ ابْنِ عُمَرَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا : أَنَّ النَّبِيَّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ كَانَ إِذَا وَضَعَ الْمَيِّتَ فِي الْقَبْرِ، قَالَ : بِسْمِ اللَّهِ ، وَعَلَى سُنَّةِ رَسُولِ اللَّهِ . (١)

٢٠ - الدُّعَاءُ عِنْدَ إِفْطَارِ الصَّائِمِ

رَوَى أَبُو دَاوُدَ وَحَسَنَهُ الْأَلْبَانِيُّ عَنْ ابْنِ عُمَرَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا قَالَ " كَانَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ إِذَا أَفْطَرَ،

قَالَ : ذَهَبَ الظَّمَأُ وَابْتَلَّتِ الْعُرُوقُ وَثَبَتَ الْأَجْرُ إِنْ شَاءَ اللَّهُ " . (٢)

٢١ - الدُّعَاءُ لِمَنْ سَمِعَ نُبَاحَ الْكِلَابِ بِاللَّيْلِ

رَوَى أَبُو دَاوُدَ وَهُوَ حَسَنٌ بِطَرَفِهِ عَنْ جَابِرِ بْنِ عَبْدِ اللَّهِ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا ، قَالَ : قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ :

(١) صحيح : رواه أبو داود (٢٧٩٨) والترمذي (١٠٤٦) وحسنه

(٢) حسن : رواه أبو داود (٢٠١٠) وحسنه الألباني (٢٣٥٧)

19. Pemphero Lonena Poika Maliro Mmanda

Nkhani nachokera kwa Abu Daud ndipo anamva kuchokera kwa Ibn Umar, Mulungu asangalale nawo, anati: Pamene Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anali kuika maliro mmanda, anali kunena kuti: "Bismillah, Wa'ala sunnati Rasuli Llah" Abu Daud 3798 – At Tirmidh 1046

20. Pemphero Lonena Pamene Osala akumasula

Nkhani inachokera kwa Abu Daud ndipo Al-Baani anaivomereza kuti ndiyoona, anamva kuchokera kwa Ibn Umar, Mulungu asangalale naye, anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye amati akamasula kusala amanena kuti: "Dhahaba dhamau wabtallatil urooq wathabatal ajru in-sha-Allah" Abu Daud 2010 – Al Albani 2357

21. Pemphero Lonena Yemwe Wamva Kukuwa kwa Galu Usiku

Nkhani inachokera kwa Abu Daud, anamva kuchokera kwa Jabir ibn Abdullah, Mulungu asangalale nawo, anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati:

"Mukamva kukuwa kwa agalu kapena kulira kwa abulu usiku, zitchinjirizeni kwa Mulungu, chifukwa iwowo amakhala akuwona zomwe inu simukuona" Abu Daud 4460 – Al Albani 5103

## 22. Pemphero Kwa Odwala Pamene Tamuyendera

Nkhani inachokera kwa At Tirmidhi, anamva kuchokera kwa Ibn Abbas Mulungu asangalale naye, anamva kwa Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye akunena kuti: "Kapolo wa Chisilamu yemwe angayendere odwala nthawi yomwalira isanakwane,

ndikunena kuti:

'As'alu Allahal Adheem, Rabbal Arshil Adheem, an yashfiyaka', kokwana kasanu ndi kawiri, Mulungu amamchiritsa" At Tirmidhi 2083 – Al Albani 5766

## 23. Pemphero Lonena Pakati pa kukhala kuwiri (Pa Swalat)

Nkhani inachokera kwa At Tirmidhi, ndipo Al-Baani anaivomereza kuti ndiyoona, anamva kuchokera kwa Abbas Mulungu asangalale naye, anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anali kunena mau awa pakati pa kukhala kuwiri: "Allahumma ighfir li, warhamni, wajubrini, wahdini, warzuqni." At Tirmidhi 262 – An Nawawi 2/623 – Ahmad Shaakir "Sunan Tirmidhi 2/473" – Al Albani 284

"إِذَا سَمِعْتُمْ نُبَاحَ الْكِلَابِ وَنَهْيَ الْحُمْرِ بِاللَّيْلِ، فَتَعَوَّذُوا بِاللَّهِ، فَإِنَّهُمْ يَرَوْنَ مَا لَا تَرَوْنَ". (١)

## ٢٢- الدُّعَاءُ لِلْمَرِيضِ فِي عِيَادَتِهِ

رَوَى التِّرْمِذِيُّ وَحَسَنَهُ عَنْ ابْنِ عَبَّاسٍ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا، عَنِ النَّبِيِّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ أَنَّهُ قَالَ: "مَا مِنْ عَبْدٍ مُسْلِمٍ يَعُودُ مَرِيضًا لَمْ يَخْضُرْ أَجَلُهُ فَيَقُولُ سَبْعَ مَرَّاتٍ: أَسْأَلُ اللَّهَ الْعَظِيمَ رَبَّ الْعَرْشِ الْعَظِيمِ أَنْ يَشْفِيكَ، إِلَّا عُوِيَ" (٢)

## ٢٣- دُعَاءُ الْجَلْسَةِ بَيْنَ السَّجْدَتَيْنِ

رَوَى التِّرْمِذِيُّ وَصَحَّحَهُ الْأَلْبَانِيُّ عَنْ ابْنِ عَبَّاسٍ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا، أَنَّ النَّبِيَّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ كَانَ يَقُولُ بَيْنَ السَّجْدَتَيْنِ: اللَّهُمَّ اغْفِرْ لِي وَارْحَمْنِي وَاجْبُرْنِي وَاهْدِنِي وَارْزُقْنِي". (٣)

(١) صحيح: رواه أبو داود (٤٤٦٠) وصححه الألباني (٥١٠٣)

(٢) حسن: رواه الترمذي (٢٠٨٣) وصححه الألباني (٥٧٦٦)

(٣) صحيح: رواه الترمذي (٢٦٢) وحسنه النووي في الخلاصة (٦٢٣/٢) وأحمد شاكر في تحقيق سنن الترمذي (٤٧٣/٢)

٢٤ - دُعَاءُ رُؤْيَةِ الْهِلَالِ

رَوَى التِّرْمِذِيُّ وَحَسَنَهُ عَنْ طَلْحَةَ بْنِ عُبَيْدٍ اللَّهِ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا ، أَنَّ النَّبِيَّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ : " كَانَ إِذَا رَأَى الْهِلَالَ قَالَ : اللَّهُمَّ أَهْلُهُ عَلَيْنَا بِالْإِيمَانِ وَالْإِسْلَامِ رَبِّي وَرَبُّكَ اللَّهُ " . (١)

٢٥ - الدُّعَاءُ قَبْلَ الطَّعَامِ

رَوَى التِّرْمِذِيُّ وَقَالَ حَسَنٌ صَحِيحٌ عَنْ عَائِشَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهَا ، قَالَتْ : قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ : إِذَا أَكَلَ أَحَدُكُمْ طَعَامًا فَلْيَقُلْ بِسْمِ اللَّهِ فَإِنْ نَسِيَ فِي أَوَّلِهِ فَلْيَقُلْ بِسْمِ اللَّهِ فِي آخِرِهِ " . (٢)

٢٦ - مَا يُقَالُ لِلْكَافِرِ إِذَا عَطِسَ فَحَمِدَ اللَّهَ

رَوَى التِّرْمِذِيُّ وَقَالَ حَسَنٌ صَحِيحٌ عَنْ أَبِي مُوسَى رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ ، قَالَ : " كَانَ الْيَهُودُ يَتَعَاطِسُونَ عِنْدَ النَّبِيِّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ

(١) حسن : رواه الترمذي (٣٣٧٣) وحسنه الألباني (٤٧٢٦)

(٢) صحيح : رواه الترمذي (١٧١٨) وصححه الألباني (١٨٥٨)

24. Pemphero Lonena Poona Mwezi Watsopano

Nkhani inachokera kwa At Tirmidhi, yemwe anamva kuchokera kwa Talhata bun Ubaydah, Mulungu asangalale naye, anati: Panthawi yomwe Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye waona mwezi watsopano, anali kunena mau awa: "Allahumma ahillahu alayna bil yumni wal iman wassalamat wal Islami, Rabbi wa Rabbuka Allah." At Tirmidhi 3373 – Al Abani 4726

25. Pemphero Lonena Tisanayambe Kudya

Nkhani inachokera kwa At Tirmidhi, yemwe anamva kuchokera kwa Aisha Mulungu Asangalale naye, anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati "Mmodzi wa inu akafuna kudya anene mau awa 'Bismillah' akaiwala kumayambiliro anene kuti 'Bismillah fi awwalihi wa akhirihi'" At Tirmidhi 1718 – Al Albani 1858

26. Zoyenera kunena kwa Osakhulupilira Pamene Wayetsemua ndikunena kuti 'Ahamdulillah'

Nkhani inachokera kwa At Tirmidhi, yemwe anamva kuchokera kwa Abu Musa, Mulungu Asangalale naye, anati: "Pamene Ayuda ankayetsemula nthawi ya Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye, ankafuna kuti adzinena kwa iwo kuti:

"yarhamukumullah' ndipo iwo adzinena kuti  
'yahdikumullah wayaslih baalakum" At Tirmidhi 2663

## 27. Pemphero Lonena Kwa Mkwati

Nkhani inachokera kwa At Tirmidhi, yemwe anamva kuchokera  
kwa Abu Hurairah, Mulungu asangalale naye, anati: Pamene  
Mtumiki anali kufunira mafuno abwino kwa yemwe wakwatira,  
amanena kuti: "Baaraka Allah laka wabaaraka alaika  
wajama'a bainakumafil khayr" At Tirmidhi 1011

## 28. Pemphero Lonena Munthu Akaona Wina Yemwe ali mu Zovuta

Nkhani inachokera kwa At Tirmidhi, yemwe anamva kuchokera  
kwa Abu Hurairah, Mulungu asangalale naye, anati: Mtumiki  
Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati:  
"Yemwe waona munthu ali mzovuta ndikunena kuti  
'Alhamdulillah lhadhi 'aafaani mimma ibtalaaka bihi wa  
fadhwallani alaa kathirin mimman khalaqa tafdhwilan'  
silidzampeza vuto longa ngati limenelo" At Tirmidhi 3432 –  
Al Albani 2737.

يَرْجُونَ أَنْ يَقُولَ لَهُمْ: "يَرْحَمُكُمُ اللَّهُ، فَيَقُولُ: يَهْدِيكُمُ اللَّهُ وَيُصْلِحَ  
بَالَكُمْ. (١).

## ٢٧- الدُّعَاءُ لِلْمُتَزَوِّجِ

رَوَى التِّرْمِذِيُّ وَقَالَ حَسَنٌ صَحِيحٌ عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ، أَنَّ  
النَّبِيَّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ كَانَ إِذَا رَفَأَ<sup>(١)</sup> الْإِنْسَانَ إِذَا تَزَوَّجَ،

قَالَ: بَارَكَ اللَّهُ لَكَ وَبَارَكَ عَلَيْكَ وَجَمَعَ بَيْنَكُمَا فِي الْخَيْرِ. (٣).

## ٢٨- دُعَاءُ مَنْ رَأَى مُبْتَلًى

رَوَى التِّرْمِذِيُّ وَحَسَنُهُ عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ قَالَ: قَالَ رَسُولُ اللَّهِ  
صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ مَنْ رَأَى مُبْتَلًى فَقَالَ الْحَمْدُ لِلَّهِ الَّذِي عَافَانِي بِمَا  
ابْتَلَاكَ بِهِ وَفَضَّلَنِي عَلَى كَثِيرٍ مِمَّنْ خَلَقَ تَفْضِيلًا لَمْ يُصِبْهُ ذَلِكَ الْبَلَاءُ"

(١).

(١) صحيح: رواه الترمذي (٢٦٦٣) وقال حسن صحيح

(٢) رَفَأَ: هَنَأَ ودَعَا لَهُ

(٣) صحيح: رواه الترمذي (١٠١١) وقال حسن صحيح

٢٩ - الدُّعَاءُ لِمَنْ صَنَعَ إِلَيْكَ مَعْرُوفًا

رَوَى التِّرْمِذِيُّ وَحَسَنَهُ عَنْ أُسَامَةَ بْنِ زَيْدٍ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ ، قَالَ : قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ : " مَنْ صُنِعَ إِلَيْهِ مَعْرُوفٌ فَقَالَ لِفَاعِلِهِ : جَزَاكَ اللَّهُ خَيْرًا فَقَدْ أَبْلَغَ فِي الشَّنَاءِ " (١)

٣٠ - دُعَاءُ الْمُقِيمِ لِلْمُسَافِرِ

رَوَى التِّرْمِذِيُّ وَقَالَ حَسَنٌ صَحِيحٌ عَنْ ابْنِ عُمَرَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا ، كَانَ يَقُولُ لِلرَّجُلِ إِذَا أَرَادَ سَفَرًا : اذْنُ مِنِّي أَوْدَعَكَ كَمَا كَانَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ يُودِّعُنَا ، فَيَقُولُ : اسْتَوْدِعْ اللَّهَ دِينَكَ وَأَمَانَتَكَ وَخَوَاتِيمَ عَمَلِكَ " (٢)

(١) صحيح : رواه الترمذي (١٩٥٨) وقال حسن جيد غريب ثم روى عن المكي بن إبراهيم قال كنا عند ابن جريج المكي فجاء سائل فسأله فقال ابن جريج لحازنه أعطه دينارًا فقال ما عندي إلا دينار إن أعطته طغيت وعمالك قال فغضب وقال أعطه قال المكي فنحن عند ابن جريج إذ جاء رجل بكتاب وصورة وقد بعث إليه بعض إخوانه وفي الكتاب إلى قد بعثت حسين دينارًا قال فحمل ابن جريج الصورة فعدّها فإذا هي أحد وخمسون دينارًا قال فقال ابن جريج لحازنه قد أعطيت واحدًا فردّه الله عليك وزادك حسين دينارًا

(٢) صحيح : رواه أبو داود (٣٣٦٥) وصححه الألباني (٢٦٠٠)

29. emphelo Lonena Yemwe Wachitiridwa Zabwino

Nkhani inachokera kwa At Tirmidhi, yomwe inatsimikizidwa ubwino wake ndi Usamah, Mulungu asangalale naye, anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati: "Yemwe wachitiridwa zabwino ndikunena kwa ochitayo mau awa: 'Jazaaka Allah Khayran' ndiye kuti wakwanitsa kuyamika" At Tirmidhi 1958

30. Pemphero Lonena Otsala Wapaulendo kwa Opita ku Ulendo

Nkhani inachokera kwa At Tirmidhi, ndipo anatsimikiza kuti ndi yabwino, anamva kuchokera kwa Umar, Mulungu asangalale nawo, amati akaona munthu yemwe akufuna ulendo, amanena kuti: "Ndiyandikire ndisanzikane nawe monga mmene Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anali kutsanzikirana nafe, ndipo amati: "Astawdi'u Llaaha dinaka wa amaanataka wa khawaatiima 'amalika" Abu Daud 3365. - Al Albani 2600

٣١- مَا يَفْعَلُ مَنْ آتَاهُ أَمْرٌ يَسْرُهُ

رَوَى التِّرْمِذِيُّ وَحَسَنَهُ عَنْ أَبِي بَكْرَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ، أَنَّ النَّبِيَّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ: "كَانَ إِذَا آتَاهُ أَمْرٌ يَسْرُهُ أَوْ بُشِّرَ بِهِ، خَرَّ سَاجِدًا شُكْرًا لِلَّهِ تَبَارَكَ وَتَعَالَى". (١)

٣٢- مَا يُقَالُ عِنْدَ الذَّبْحِ أَوْ النَّحْرِ

رَوَى التِّرْمِذِيُّ وَصَحَّحَهُ الْأَلْبَانِيُّ عَنْ جَابِرِ بْنِ عَبْدِ اللَّهِ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا، قَالَ: "شَهِدْتُ مَعَ النَّبِيِّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ الْأَضْحَى بِالْمُصَلَّى، فَلَمَّا قَضَى خُطْبَتَهُ نَزَلَ عَنْ مَنْبَرِهِ، فَأَتَى بِكَبْشٍ فَذَبَحَهُ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ بِيَدِهِ، وَقَالَ بِسْمِ اللَّهِ أَكْبَرُ، هَذَا عَنِّي وَعَمَّنْ لَمْ يُضَحَّ مِنْ أُمَّتِي". (١)

(١) حسن: رواه الترمذي (١٥٧٨) وقال حسن غريب وحسنه الألباني (١٤١٤)

صحیح: رواه الترمذي (١٤٨١) وصححه الألباني

### 31. Zoyenera Kuchita Yemwe Chamufikira Chinthu Chosangalatsa

Nkhani inachokera kwa At Tirmidhi, yomwe inatsimikizidwa ubwino wake, kuchokera kwa Abi Bakrata, Mulungu asangalale naye, anati: Pa nthawi yomwe chamufikira Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye chinthu chosangalatsa, anali kupanga sijdah, kuyamika Mulungu." At Tirmidhi 1578 – Al Albani 1414

### 32. Zoyenera Kunena Pozinga

Nkhani inachokera kwa At Tirmidhi, yomwe anatsimikiza ubwino wake Al Albaani, kuchokera kwa Jabir bin Abdullah, Mulungu asangalale nawo, anati: "Ndinakhala ndi Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye, pa (Eidul) Adh'ha mumzikiti, pamene anamaliza khutbah yake, anatsika pa min'bari ndipo inabweretsedwa nkhoa kwa iye yomwe anaizinga ponena mau awa: "Bismillah Allah Akbar, (kuzingaku) ndi kwa ine ndi yense yemwe sanazinge mu Ummah wanga" At Tirmidhi 1481

وَفِي الصَّحِيحَيْنِ عَنِ الْبَرَاءِ بْنِ عَازِبٍ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ، قَالَ : قَالَ النَّبِيُّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ : " إِذَا أَتَيْتَ مَضْجَعَكَ فَتَوَضَّأْ وَضُوءَكَ لِلصَّلَاةِ، ثُمَّ اضْطَجِعْ عَلَى شِقِّكَ الْأَيْمَنِ، ثُمَّ قُلْ : اللَّهُمَّ أَسْلَمْتُ وَجْهِيَ إِلَيْكَ، وَفَوَّضْتُ أَمْرِي إِلَيْكَ، وَأَلْجَأْتُ ظَهْرِي إِلَيْكَ رَغْبَةً وَرَهْبَةً إِلَيْكَ، لَا مَلْجَأَ وَلَا مَنْجَا مِنْكَ إِلَّا إِلَيْكَ، اللَّهُمَّ آمَنْتُ بِكِتَابِكَ الَّذِي أَنْزَلْتَ وَبِنَبِيِّكَ الَّذِي أَرْسَلْتَ، فَإِنْ مِتُّ مِنْ لَيْلَتِكَ فَأَنْتَ عَلَى الْفِطْرَةِ، وَاجْعَلْهُنَّ آخِرَ مَا تَتَكَلَّمُ بِهِ " (١)

٣٤ - ذِكْرُ الرُّجُوعِ مِنَ السَّفَرِ

فِي الصَّحِيحَيْنِ عَنْ عَبْدِ اللَّهِ بْنِ عُمَرَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا، " أَنَّ رَسُولَ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ كَانَ إِذَا قَفَلَ مِنْ غَزْوٍ أَوْ حَجٍّ أَوْ عُمْرَةٍ يُكَبِّرُ عَلَى كُلِّ شَرْفٍ مِنَ الْأَرْضِ ثَلَاثَ تَكْبِيرَاتٍ، ثُمَّ يَقُولُ

(١) صحيح : رواه البخاري (٢٣٩) ومسلم (٤٨٨٤)

33. Mau Onena Pogona

Kuchokera kwa Al Bukhari ndi Muslim, Al Barraa bun 'Aazib anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati: "Ukafika pogona, panga wudhu monga mmene umapangira wudhu ukafuna kuswali, kenako gona mbali yaku manja ndipo unene mau awa 'Allahumma aslamtu wajhiy ilaika, wa sawwadhtu amri ilaika, wa alja'tu dhwahri ilaika raghbatan wa rahbatan ilaika. Laa malja'a wala man'ja'a minka illa ilaika. Allahumma aamantu bikitaabika alladhi anzalta WA binabiyyika alladhi arsalta' ndipo ukamwalira usiku umenewo, wamwalira uli mu njira ya Mulungu, ndipo uwapange mau amenewa kukhala mau omaliza kuyankhula" Al Bukhari 239 – Muslim 4884

34. Zoyenera Kuyankhula Pobwelera ku Ulendo

Kuchokera kwa Al Bukhari ndi Muslim, Ibn Umar Mulungu asangalale nawo anati: "Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye amati akamaliza nkhondo, Hajj kapena Umrah, ankapanga ma takbirah atatu, kenako amanena kuti:

**"Laa ilaaha illa Allah wahdahu laa**

**sharika lahu, lahul mulku walahul hamdu wa huwa 'alaa  
kulli shay'in qadeer, aayiboona taaiboon 'aabidoon  
saajidoon lirabbinaa haamidoon, swadaqa Allah wa'dahu  
wanaswara 'abdahu wahazamal ahzaaba wahdahu" Al  
Bukhari 1670 – Muslim134**

### **35. Pemphero Lonena Potsegulira (Swalat)**

Nkhani inachokera kwa Al Bukhari, yemwe anamva kuchokera  
kwa Abu Hurairah Mulunguasangalale naye: Mtumiki Mtendere  
ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anali kukhala chete  
pakati pa Takbeer ndi kuwerenga (kwa Surat Al Fatihah)  
kukhala chete kwenikweni, ndipo ine ndinati: Ee Mtumiki, kodi  
mukumanena chani mukakhala chete pakati pa Takbeer ndi  
kuwerenga? Ndipo anati: "Ndimanena kuti: 'Allahumma  
baa'id bayni wa bayna khatwaayaay kamaa baa'dta baynal  
mashriq wal maghrib. Allahumma naqqini minal khatwaay  
kamaa yunakka thawbul abyadh mina ddanas.  
Allahummaghsil khatwaayaay bil maai wa thhalji wal  
bardi'" Al Bukhari 723

"لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ وَحْدَهُ لَا شَرِيكَ لَهُ، لَهُ الْمُلْكُ وَلَهُ الْحَمْدُ وَهُوَ عَلَى كُلِّ  
شَيْءٍ قَدِيرٌ آيُونَ تَائِبُونَ عَابِدُونَ سَاجِدُونَ لِرَبِّنَا حَامِدُونَ صَدَقَ اللَّهُ  
وَعْدَهُ وَنَصَرَ عَبْدَهُ وَهَزَمَ الْأَحْزَابَ وَحْدَهُ". (١)

### **٣٥- دُعَاءُ الْاسْتِفْتَاَحِ**

رَوَى الْبُخَارِيُّ عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ قَالَ كَانَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ  
عَلَيْهِ وَسَلَّمَ يَسْكُتُ بَيْنَ التَّكْبِيرِ وَبَيْنَ الْقِرَاءَةِ إِسْكَاتَةً فَقُلْتُ يَا أُمِّي يَا  
رَسُولَ اللَّهِ إِسْكَاتُكَ بَيْنَ التَّكْبِيرِ وَالْقِرَاءَةِ مَا تَقُولُ قَالَ أَقُولُ اللَّهُمَّ بَاعِدْ  
بَيْنِي وَبَيْنَ خَطَايَايَ كَمَا بَاعَدْتَ بَيْنَ الْمَشْرِقِ وَالْمَغْرِبِ اللَّهُمَّ نَقِّنِي مِنْ  
الْخَطَايَا كَمَا يُنْقَى الثَّوْبُ الْأَبْيَضُ مِنَ الدَّنَسِ اللَّهُمَّ اغْسِلْ خَطَايَايَ بِالْمَاءِ  
وَالثَّلْجِ وَالْبَرَدِ. (٢)

(١) صحيح : رواه البخاري (١٦٧٠) ومسلم (١٣٤٤)

(٢) صحيح رواه البخاري (٧٢٣)

36. Pemphero Lonena Popempha Kusankha Pakati pa Zinthu Ziwiri

Nkhani inachokera kwa Al Bukhari, yemwe anamva kuchokera kwa Jabir, Mulungu asangalale naye, anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anali kutiphunzitsa kupempha kusankha pakati pa zinthu ziwiri pa chirichonse, monga mmene anali kutiphunzitsira Surat ya mu Qur'an: "Munthu chikamuvuta chinthu, apange ma rak'at awiri ndipo anene mau awa: 'Allahumma inni astakhiruka bi'ilmika, wa astaqdiruka biqudratika, wa as'aluka min fadhlikal adheem, fa innaka taqdiru walaa aqdir, wa ta'lam walaa a'lam, wa anta 'allaamul ghuyoob. Allahumma in kunta ta'lam anna hadhal amra khayrun lii fi deeni wa ma'aashi wa'aaqibati amri, kapena fi 'aajil amri, wa aajilihi, faqdirhu li, wa in kunta ta'lam anna hadhal amra sharrun lii fi deeni wa ma'aashi, wa 'aaqibati amri, kapena fi 'aajil amri, wa aajilihi, faswrihu 'anni waswifni 'anhu, waqdur li alkhayra haithu kaana, thumma raddhwini bihi' ndipo atchule vuto lake" Al Bukhari 1096

٣٦- دُعَاءُ الاسْتِخَارَةِ

رَوَى الْبُخَارِيُّ عَنْ جَابِرِ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ، قَالَ : كَانَ النَّبِيُّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ يُعَلِّمُنَا الاسْتِخَارَةَ فِي الْأُمُورِ كُلِّهَا، كَالسُّورَةِ مِنَ الْقُرْآنِ : " إِذَا هَمَّ بِالْأَمْرِ فَلْيَرْكَعْ رَكَعَتَيْنِ، ثُمَّ يَقُولُ : اللَّهُمَّ إِنِّي أَسْتَخِيرُكَ بِعِلْمِكَ ، وَأَسْتَقْدِرُكَ بِقُدْرَتِكَ، وَأَسْأَلُكَ مِنْ فَضْلِكَ الْعَظِيمِ، فَإِنَّكَ تَقْدِيرُ وَلَا أَقْدِرُ، وَتَعْلَمُ وَلَا أَعْلَمُ، وَأَنْتَ عَلَامُ الْغُيُوبِ، اللَّهُمَّ إِنْ كُنْتَ تَعْلَمُ أَنَّ هَذَا الْأَمْرَ خَيْرٌ لِي فِي دِينِي وَمَعَاشِي وَعَاقِبَةِ أَمْرِي، أَوْ قَالَ فِي عَاجِلِ أَمْرِي، وَآجِلِهِ، فَأَقْدِرْهُ لِي، وَإِنْ كُنْتَ تَعْلَمُ أَنَّ هَذَا الْأَمْرَ شَرٌّ لِي فِي دِينِي وَمَعَاشِي وَعَاقِبَةِ أَمْرِي، أَوْ قَالَ فِي عَاجِلِ أَمْرِي، وَآجِلِهِ، فَاصْرِفْهُ عَنِّي وَاصْرِفْنِي عَنْهُ، وَأَقْدِرْ لِي الْخَيْرَ حَيْثُ كَانَ، ثُمَّ رَضِّنِي بِهِ وَيُسَمِّي حَاجَتَهُ (١)."

(١) صحيح : رواه البخاري (١٠٩٦)

### 37. Mau Onena Kummawa ndi Kumazulo

Nkhani inachokera kwa Al Bukhari, yemwe anamva kuchokera kwa Abu Hurairah, Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati: "Yemwe anganene mau awa 'Laa ilaaha illa Allah wahdahu laa shareeka lahu, lahul mulku walahul hamd wahuwa 'alaa kulli shay'in qadeer' kokwana zana limodzi (100) tsiku lirilonse, adzalipidwa mofanana ndi kumasula akapolo khumi (10), ndipo alembedwa zabwino zana limodzi (100) komanso machimo ake okwana zana limodzi (100) afafanizidwa, ndipo akhala otetezedwa kwa satana pa tsiku limenelo kufikira mazulo ake, ndipo palibe yemwe angapange chabwino pa tsiku limenelo choposa chimene wapanga icye." Al Bukhari 3050

### 38. Mau Otetezera Ana ku Satana

Nkhani inachokera kwa Al Bukhari, yemwe anamva kuchokera kwa Ibn Abbas, Mulungu asangalale nawo, anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anali kumuteteza Al Hassan ndi Al Hussain ku satana ndipo amawauza kuti: "Ndithu bambo anu (Ibrahim) anali kuteteza Ismail ndi Is'haq ndi mau amenewa: 'A'udhu bikalimaati Llaahi taammah min kulli shaytanin wa haammatin wa min kulli 'ainin laamma'" Al Bukhari 3207

### ٣٧- أَذْكَارُ الصَّبَاحِ وَالْمَسَاءِ

وَرَوَى الْبُخَارِيُّ عَنْ أَبِي هُرَيْرَةَ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ أَنَّ رَسُولَ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ قَالَ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ وَحْدَهُ لَا شَرِيكَ لَهُ لَهُ الْمُلْكُ وَلَهُ الْحَمْدُ وَهُوَ عَلَى كُلِّ شَيْءٍ قَدِيرٌ فِي يَوْمٍ مِائَةَ مَرَّةٍ كَانَتْ لَهُ عَذَلٌ عَشْرٌ رِقَابٍ وَكُتِبَتْ لَهُ مِائَةُ حَسَنَةٍ وَنُحِيتَ عَنْهُ مِائَةُ سَيِّئَةٍ وَكَانَتْ لَهُ حِرْزًا مِنَ الشَّيْطَانِ يَوْمَهُ ذَلِكَ حَتَّى يُنْسِيَ وَلَمْ يَأْتِ أَحَدٌ بِأَفْضَلَ مِمَّا جَاءَ بِهِ إِلَّا أَحَدٌ عَمِلَ أَكْثَرَ مِنْ ذَلِكَ. (١)

### ٣٨- مَا يُعَوَّذُ بِهِ الْأَوْلَادُ

رَوَى الْبُخَارِيُّ عَنْ ابْنِ عَبَّاسٍ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا، قَالَ: "كَانَ النَّبِيُّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ يُعَوَّذُ الْحَسَنَ وَالْحُسَيْنَ، وَيَقُولُ: إِنَّ أَبَاكُمَا كَانَ يُعَوَّذُ بِهَا إِسْمَاعِيلَ وَإِسْحَاقَ أَعُوذُ بِكَلِمَاتِ اللَّهِ التَّامَّةِ مِنْ كُلِّ شَيْطَانٍ وَهَامَّةٍ وَمِنْ كُلِّ عَيْنٍ لَامَّةٍ." (٢)

(١) صحيح: رواه البخاري (٣٠٥٠)

(٢) صحيح: رواه البخاري (٣٢٠٧)

### 39. Mau Onena Pakutha Udhu

Nkhani inachokera kwa Muslim, yemwe anamva kuchokera kwa 'Uqbah bin 'Aamir, Mulungu asangalale naye, anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anti: "Palibe mwa inu yemwe angapange wudhu mokwaniritsa ndikunena mau awa: 'Ash'hadu an laa ilaaha illa Allah wahdahu laa sharika lahu, wa ash'hadu anna Muhammadan 'abduh wa rasuluhu' popanda kumutsegulira makomo asanu ndi atatu (8) a ku Mtendende, ndipo adzalowera khomo lomwe iye adzafune" Muslim 234

### 40. Mau Onena Polowa Mnyumba

Nkhani inachokera kwa Muslim, yemwe anamva kuchokera kwa Jabir bin Abdullah, Mulungu asangalale nawo, anamva Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye akunena kuti: "Munthu akamalowa mnyumba ndi kutchula dzina la Mulungu polowapo komanso pakudya, shaytan amayankhula (modandaula) kwa anzake kuti: 'Palibe kukhala mnyumba iyi usikuwu komanso palibe chakudya chanu mnyumba iyi' ndipo akalowa mnyumbamo popanda kutchula dzina la Mulungu, shaytan amayankhula kwa anzake kuti: 'mwapeza pokhala usikuwu'", ndipo akapanda kutchula dzina la Mulungu pakudya, shaytan amayankhula kwa anzake kuti: 'mwapeza pokhala ndi chakudya usikuwu' Muslim 2018

### ٣٩- الذِّكْرُ بَعْدَ الْوُضُوءِ

رَوَى مُسْلِمٌ عَنْ عُقْبَةَ بْنِ عَامِرٍ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ قَالَ قَالَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ مَا مِنْكُمْ مِنْ أَحَدٍ يَتَوَضَّأُ فَيَسْبِغُ الْوُضُوءَ ثُمَّ يَقُولُ أَشْهَدُ أَنْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ وَحْدَهُ لَا شَرِيكَ لَهُ وَأَشْهَدُ أَنَّ مُحَمَّدًا عَبْدُهُ وَرَسُولُهُ إِلَّا فُتِحَتْ لَهُ أَبْوَابُ الْجَنَّةِ الثَّمَانِيَةِ يَدْخُلُ مِنْ أَيِّهَا شَاءَ (١)

### ٤٠- الذِّكْرُ عِنْدَ دُخُولِ الْمَنْزِلِ

رَوَى مُسْلِمٌ عَنْ جَابِرِ بْنِ عَبْدِ اللَّهِ رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا أَنَّهُ سَمِعَ النَّبِيَّ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ يَقُولُ إِذَا دَخَلَ الرَّجُلُ بَيْتَهُ فَذَكَرَ اللَّهَ عِنْدَ دُخُولِهِ وَعِنْدَ طَعَامِهِ قَالَ الشَّيْطَانُ لَا مَبِيتَ لَكُمْ وَلَا عَشَاءَ وَإِذَا دَخَلَ فَلَمْ يَذْكُرِ اللَّهَ عِنْدَ دُخُولِهِ قَالَ الشَّيْطَانُ أَذْرَكْتُمُ الْمَبِيتَ وَإِذَا لَمْ يَذْكُرِ اللَّهَ عِنْدَ طَعَامِهِ قَالَ أَذْرَكْتُمُ الْمَبِيتَ وَالْعَشَاءَ (٢)

(١) صحيح: رواه مسلم (٢٣٤)

(٢) صحيح: مسلم (٢٠١٨)

#### 41. Pemphero Lonena Polowa Mumzikiti

Nkhani inachokera kwa Muslim, yemwe anamva kuchokera kwa Abi Humayd, kapena Abi Usayd, Mulungu asangalale naye, anati: Mtumiki Mtendere ndi Madalitso a Mulungu zikhale pa iye anati: “Mmodzi wa inu akamalowa mumzikiti, anene mau awa: ‘Allahumma iftah li ab’waaba rahmatika’ ndipo akamatuluka, anene mau awa: ‘Allahumma inni as’aluka min fadhlika’” Muslim 713

#### 42. Mau Onena Nthawi ya Adhan

